pawo, Mulungu anaŵapulumutsa anthu amene anamu-
khulupilira Iye.



PHUNZIRO LA 37

1. Kodi ndani amene analemba mabuku asano oyambirira a m'buku la Mulungu, Bayibulo?
-Mose.

2. Kodi Mose anazidziŵa bwanji zakuti alembe?
-Mulungu anamutsogolera Mose kulemba zimene Iye ankafuna kuti Moseyo alembe.

3. Kodi a Isirayeli ankayidziŵa bwanji njira pamene iwowo ankayenda mchipululu muja?
-Mulungu ankaŵatsogolera a Isirayeliwo.

4. Kodi Mulungu ankaŵatsogolera bwanji a Isirayeli pa nthaŵ\i ya masana ndi usiku?
-Mulungu ankaŵatsogolera a Isirayeli ndi mtambo pa nthaŵi ya masana.
-Mulungu ankaŵatsogolera a Isirayeli ndi chipilala cha moto pa nthaŵi ya usiku.

5. Kodi Mulungu ankaŵatsogolera a Isirayeli kupita kuti?
-Mulungu ankaŵatsogolera a Isirayeli kupita ku dziko la Kanani, limene analilonjeza Mulungu kwa kholo lawo, Abulahamu.

6. A Isirayeli atafika ku malire a dziko la Kanani, kodi Mulungu anamuwuza Musa kuti achite chiyani?
-Mulungu anamuwuza Musa kuti asankhe amuna 12, m'modzi ku mtundu uliwonse pa mitundu 12 ija, kuti apite kukalizonda dziko la Kanani.

7. Kodi chifukwa chiyani amuna khumi amene samkamukhulupilira Mulungu aja sankafuna kulowa mu dziko la kanani?
-Amuna khumi amene samkamukhulupilira Mulungu aja

nkaŵawopa anthu akuluakulu ndiponso a mphamvu amene ankakhala mu dziko la kanani lija.
-Amuna khumi amene samkamukhulupilira Mulungu aja, sankakhulupilira kuti Mulungu anapereka lonjezo kwa a Isirayeli loŵapatsa dziko la Kanani.
-Amuna khumi amene samkamukhulupilira Mulungu aja, sankakhulupilira kuti Mulungu anali wa mphamvu kwambiri mwakuti anakatha kuŵagonjetsa anthu amene ankakhala mu dziko la Kanani lija.

8. Kodi chifukwa chiyani Kalebe ndi Yoswa ankafuna kuloŵa mu dziko la Kanani?
-Kalebe ndi Yoswa sankaŵawopa anthu akuluakulu ndiponso a mphamvu amene amkakhala mu dziko la Kanani.
-Kalebe ndi Yoswa ankakhulupilira kuti Mulungu asunga pangano lache ndi kuŵapatsa a Isirayeli dziko la Kanani.
-Kalebe ndi Yoswa ankakhulupilira kuti Mulungu anali ndi mphamvu zambiri mwakuti anakatha kuŵagonjetsa anthu amene ankakhala mu dziko la Kanani.

9. Ngati sitikukhulupilira mawu a Mulungu ndiye kuti ife tikumutcha Mulungu kuti ndi otani?
-Wabodza.

10. Kodi ndani amene adzaloŵe mu dziko la Kanani chifukwa chakuti a Isirayeli sanamukhulupilire Mulungu?
-Yoswa, Kalebe ndi ana awo okha ndi amene adzaloŵe mu dziko la Kanani.

11.Kodi Mulungu anapereka chilango chotani kwa a Isirayeli chifukwa chakuti a Isirayeliwo sanamukhulupilire Mulungu?
-A Isirayeli sadzaloŵa mu dziko la Kanani.

-Chifukwa chakuti a Isirayeli sanamukhulupilire Mulungu,



imene anayipachika pa mtengo ija, anachira?
-Inde.

-Kodi a Isirayeli anakangopemphera koma osayang'ana pa mtengo wa mkuwa uja, anakachira?
-Iyayi.

-A Isirayeli amayenera kumvera zimene analankhula Mulungu kuti apulumutsidwe.
-A Isirayeli amayenera kutsata njira ya Mulungu kuti apulumutsidwe.
-A Isirayeli ankayenera kuyang'ana pa njoka imene inapachikidwa pa mtengo ija kuti apulumutsidwe.

-Kodi a Isirayeli amene anayang'ana pa njoka ya mkuwa imene anayipachika pa mtengo ija, anafa?
-Iyayi.
-Kodi njoka ya mkuwa ija, inali ndi mphamvu zina zilizonse zoŵapulumutsira a Isirayeli?
-Iyayi.
-Kodi ndani yekha amene anali ndi mphamvu zoŵapulumutsira a Isirayeli?
-Mulungu.

-Mulungu amasunga malonjezo ache nthaŵi zonse.
-Mulungu anaŵapulumutsa a Isirayeli onse amene anayang'ana pa njoka ya nkuwa imene anayipachika pa mtengo ija.

-Kodi tchimo la a Isirayeli linayitanitsa imfa?
-Inde.

-Ngakhale kuti tchimo la a Isirayeli linayitanitsa imfa pakati pawo, Mulungu anali ndi chisoni kwambiri.

-Ngakhale kuti tchimo la a Isirayeli linayitanitsa imfa pakati

-Kodi a Isirayeli anakatha kudzipulumutsa okha kwa njoka za ululu zija?
-Iyayi.

-Kodi ndani yekha amene anakatha kuŵapulumutsa a Isirayeli aja ku njoka za ululu zija?
-Mulungu.

-Kodi Mulungu anaŵathandiza a Isirayeli?

Tiyeni tiŵerenge Numeri 21:8-9a

8-Kenako Ambuye anamuwuza Mose kuti, “ Upange njoka ya mkuwa ndipo uyipachike pa mtengo, kuti aliyense amene walumidwa adzitha kuyiwona ndi kukhala ndi moyo.”
9-Chomcho Mose anapanga njoka ya mkuwa ndikuyipachika pa mtengo.

-Kodi Mulungu anamuwuza Mose kuti achite chiyani pofuna kuŵapulumutsa a Isirayeli?
-Anamuwuza kuti apange njoka ya mkuwa ndipo ayipachike pa mtengo.

-Kodi a Isirayeli amene amkafuna kuti apulumuke, amayenera kuchita chiyani?
-Kuyang’ana pa njoka ya mkuwa imene anayipachika pa mtego ija.

Tiyeni tiŵerenge Numeri 21:9b

9-Aliyense amene analumidwa, anakhala ndi moyo atayang’ana pa njoka ya mkuwayo.

-Kodi a Isirayeli amene ankayang’ana pa njoka ya mkuwa



iwowo sanaloŵe mu dziko la Kanani, ndipo ankangozungulirazungulira mchipululu.

-A Isilayeli atafika ku Kadeshi, kunalibe madzi.

-Kodi mukuganiza kuti a Isirayeli anachita chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Numeri 20:1-5

1-Pa mwezi oyamba, khamu lonse la a Isirayeli linafika ku chipululu cha Sini ndipo linamanga masakasa awo ku Kadeshi. Miriyamu anafera komweko ndiponso anamuyika komweko.
2-Kumene anamanga masakasa awoko, kunalibe madzi, chomcho anthu anasonkhana ndi kumuzungulira Mose ndi Aroni.
3-Kenako anayamba kukangana ndi Mose ndipo anati, “Zinakakhala bwino tinakafera pa maso pa Ambuye pamodzi ndi a Isirayeli amzathu aja.
4-Kodi chifukwa chiyani mwalitengera khamu la Ambuyeli ku chipululu kuno? Mwangofuna kuti Ife tifere kuno pamodzi ndi nyama zathuzi?
5-Kodi chifukwa chiyani munatiturutsa ife mu dziko la Iguputo ndikutibweretsa ku malo oyipa kuno? Malo opanda mbewu ina iliyonse, mkuyu, mpesa ngakhale makangaza ndi madzi akumwa.

-Kodi pamene a Isirayeli analibe madzi, iwowo anakhulupilira mwa Mulungu kuti aŵapatsa madzi?
-Iyayi.

-Kodi nanga a Isirayeli anapanga chiyani?
-A Isirayeli ankamunena Mose ndi Aroni.

-Kodi a Isirayeli anakachita chiyani pamene iwowo analibe madzi?

-A Isirayeli anakamupempha Mulungu kuti aŵapatse madzi.

-Poyamba Mulungu anaŵapatsa a Isirayeli madzi kuchokera mu tanthwe.
-Kodi nanga chifukwa chiyani a Isirayeli sanamupemphe Mulungu kuti aŵapatse madzi?
-Chifukwa chakuti sankakhulupilira mwa Mulungu.

-Ngakhale masiku ano, anthu ambiri ali ngati a Isirayeli.
-Ngakhale kuti Mulungu amaŵapatsa mvura, ndikumachipangitsa chimanga kuti chidzimera, ambiri mwa anthufe sitikhulupilirabe mwa Iye.

-Kodi Mose ndi Aroni anapanga chiyani madzi atasoŵa?

Tiyeni tiŵerenge Numeri 20:6

6-Mose ndi Aroni anachoka kumene anayima anthuko ndipo anapita pa khomo la chihema chokumanilanamo. Anagwetsa nkhope zawo pansi, ndipo ulemelero wa Ambuye unaŵawonekera.

-Mose ndi Aroni anakhulupilira mwa Mulungu.
-Mose ndi Aroni anapempha kwa Mulungu kuti aŵapatse mvura.

-Kodi Mose ndi Aroni anakatha kuŵapatsa a Isirayeli madzi?
-Iyayi.
-Kodi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti iwowo anali mchipululu.

-Kodi Mulungu anakasankha zosaŵapatsa a Isirayeli madzi, kodi chinakachitika ndichiyani?
-A Isirayeli onse anakafa.



thaŵire.

-Mu nthaŵi ya Nowa,  kodi panali malo akuti anthu amene anali kunja kwa chombo chija anakatha kuthaŵira?
-Panalibe.

-Mu nthaŵi ya Sodomu ndi Gomora, kodi panali malo akuti anthu amene anali mkati mwa mzinda uja anakatha kuthaŵira?
-Panalibe.

-Kodi mkazi wache wa Loti anachithaŵa chilango cha Mulungu chija pamene iye anatembenukira kumbuyo ndikuyiyang'ana mizinda ija?
-Iyayi.

-Mulungu akaganiza zopereka chilango kwa anthu amene sakumukhulupilira Iye, palibenso kumene anthuwo angathaŵire.

-A Isirayeli  ambiri atafa, kodi a Isirayeli otsala aja anachita chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Numeri 21:7

7-Anthu aja anafika kwa Mose ndipo anati, “Ife tinachimwa pamene tinatsutsana ndi Ambuye pamodzi ndi iweyo. Upemphere kwa Ambuye kuti azichotse njokazo.” Chomcho Mose anaŵapempherera anthu aja.

-Kodi a Isirayeli anakuvomereza kuchimwa kwawo?
-Inde.

-Kodi a Isirayeli anamupempha Mose ndi Mulungu kuti aŵathandize iwowo?
-Inde.

ko la Edomi. Koma anayamba kudandawula ali mnjira.

5-Anayamba kutsutsana ndi Mulungu pamodzi ndi Mose. Anadandawula kuti, “Kodi mwatitulutsira chiyani ife mu dziko la Iguputo kuti tifere mchipululu muno, mulibe chakudya ndi madzi! Tikudana nazo zakudya zopanda pachezi.

-Ngakhale kuti Mulungu anapereka madzi kwa a Isirayeli, a Isirayeli anapitirizabe kudandawula.

-Chifukwa chakuti a Isirayeli anapitirizabe kudandawula, kodi Mulungu anaŵachitira chiyani a Isirayeli?

Tiyeni tiŵerenge Numeri 21:6

6-Kenako Ambuye anatumiza njoka za ululu wowopsya pakati pa a Isirayeli, zinaluma a Isirayeli ambiri ndipo anafa.

-Mulungu anaŵalanga a Isirayeli, poŵatumizira njoka za ululu zambiri .
-Njoka za ululuzo zinali paliponse.

-A Isirayeli ambiri analumidwa ndi njokazo ndipo anafa.

-Njokazo zili ngati tchimo.
-Tchimo limaŵaluma anthu ngati m’mene zinaŵalumira a Isirayeli njoka za ululu zija ndi kufa.

-Kodi a Isirayeli anatha kuzithaŵa njokazo?
-Iyayi.
-Kodi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti njoka za ululuzo zinali pena paliponse.

-Mulungu akaganiza zopereka chilango kwa anthu amene sakumukhulupilira Iye, anthuwo palibe kumene anga-



-Kodi Mulungu anasankha zoŵapatsa a Isirayeli madzi?

Tiyeni tiŵerenge Numeri 20:7-8

7-Ndipo Ambuye anati kwa Mose,
8-“Tenga ndodoyo, ndipo ulisonkhanitse khamulo; Iwe ndi m’bale wako Aroni, mulankhule kwa tanthwe limene lili pa maso pawolo, kuti liŵapatse madzi; chomcho uŵaturutsire madzi mu tanthwe ndi kumwetsa khamu la anthu ndi zoweta zawo zomwe.”

-Chifukwa chakuti Mulungu ankaŵakonda kwambiri a Isirayeli, Iye anasankha zoŵapatsa Isirayeli madzi.
-Kodi Mulungu anamulamula chiyani Mose?
-Mulungu anamulamula Mose kuti alankhule kwa tanthwe.

-Poyamba a Isirayeli akufuna madzi, Mulungu anamulamula Mose kuti akanthe tanthwe.

-Tsopano, Mulungu akumulamula Mose kuti alankhule kwa tanthwe.

-Kodi nanga Mose anachita chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Numeri 20:9-11

9-Ndipo Mose anatenga ndodoyo ndikuyichotsa pa maso pa Ambuye monga ngati m’mene Iwo anamuwuzira iye.
10-Ndipo Mose ndi Aroni analisonkhanitsa khamu la anthu lija patsogolo pa tanthwe, nalankhula nawo kuti, “Tamvani opikisana naye inu; kodi tikutulutsireni madzi mu tanthwemu?
11-Ndipo Mose anatambasura dzanja lache ndikupanda tanthwelo kaŵiri ndi ndodoyo. Ndipo madzi

ochuruka anaturukamo. Khamu lonse la anthu linamwa pamodzi ndi ziweto zawo zomwe.

-Kodi Mose analankhula kwa tanthwe?
-Iyayi.

-Kodi nanga Mose anachita chiyani?
-Mose anakantha tanthwe kaŵiri.
-Kodi chifukwa chiyani Mose anakantha tanthwelo?
-Chifukwa chakuti iye anaŵakwiyira a Isirayeli.

-Kodi Mose sanamumvere Mulungu?
-Inde.

-Kodi kenako Mulungu analankhula chiyani kwa Mose ndi Aroni?

Tiyeni tiŵerenge Numeri 20:12

12-Ndipo Ambuye analankhula kwa Mose ndi Aroni kuti, "Popeza simunandikhulupilire Ine, pondipatula Ine pa maso pa ana a Isirayeli, simudzalilowêtsa khamu la anthuli mu dziko limene ndinaŵapatsali.

-Chifukwa chakuti Mose ndi Aroni sanamumvere Mulungu, kodi Mulungu anaŵapatsa chilango iwowo?
-Inde.

-Kodi Mulungu anapereka chilango chotani kwa Mose ndi Aroni?
-Mulungu anaŵawuza iwowo kuti sadzaloŵa mu dziko la Kanani.

-Nthaŵi yakuti Aroni amwalire itakwana, Mulungu anamuwuza Mose kuti antenge Aroni ndikupita naye pamwamba pa phiri limene anaŵandikana nalo.



Tiyeni tiŵerenge Numeri 20:23-25 ndi 28

23-Phirilo linali m'malire mwa dziko la Edoni, ndipo Ambuye analankhula kwa Mose ndi Aroni kuti,
24-"Aroni sakaloŵa mu dziko limene ndinalilonjeza kwa a Isirayeli, afa, chifukwa chakuti nonse aŵiri simunalimvere lamulo langa ku Meliba.
25-Umutenge Aroni pamodzi ndi mwana wache, Eliyazara, ndipo ukwere nawo pa phiri la Holi."
28-Atafika pa phirilo, Mose anamuvura Aroni zovara zache za usembe ndikumumveka mwana wache Eliyazala. Aroni ana anafera pamwamba pa phirilo ndipo Mose ndi Eliyazara anatsika pa phirilo.

-Aroni anamwalilira pamwamba pa phiri.
-Kodi Aroni analoŵa mu dziko la Kanani?
-Iyayi.
-Kodi chifukwa chiyani Aroni sanalowê mu dziko la Kanani?
-Chifukwa chakuti iye sanamumvere Mulungu.

-Kodi Mulungu anaŵasunga mawu ache?
-Inde.
-Mulungu amasunga mawu ache nthaŵi zonse.

-Kodi amene analoŵa m'malo mwa Aroni ngati wamkulu wamsembe anali ndani?
-Eliyazara, mwana wamamuna wa Aroni.

-A Isirayeli anadandawulanso mu nthaŵi ina yache.

Tiyeni tiŵerenge Numeri 21:4-5

4-A Isirayeli anachoka ku phiri la Holi podzera mu njira yolowêra ku Nyanja Yifiira pofuna kuzungulira ku dzi-